# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

## Za kukonzedwanso mwatsopano kwa anthu kuti akhala ana a Mulungu

1. Tiyenera kuulula macimo athu
2. Tiyenera kudziwa njira
3. Tiyenera kukhulupirira kuti Yesu ndi Mpulumutsi wathu
4. Tiyenera kubadwa mwatsopano

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

**1. Tiyenera kuulula macimo athu**

*Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse – 1 Yohane 1.9*

**Kuwerenga**
Luka 15.1-10

**Malongosoledwe**
Mulungu ndi woyera, wamkulu kwambiri ndi wopambana. Ife ndife ang'ono ndi ocimwa. Ife si ndife abwino; nthawi zambiri sitimvera Mulungu. Timayenda pa njira zathu.
Komabe Mulungu atiitana kukhala ana ake! Kodi tisanduke bwanji ana ake?
Nthawi ina Yesu anauza nthano ya mwana wamuna wosiya nyumba yake. Kunyumba kwake kunali kwabwino, koma sanakondwereko. Sanakonde tate wake.
Tsiku lina mwanayo anati kwa tate wake, 'Ndipatseni zonse zimene zidzakhala zanga mutamwalira'.
Tate sanakondwere. Ndipo sanafune mwana wake wa mwamuna kusiya nyumba. Koma anampatsa ndalama zake. Ndipo mnyamata anacokapo.
Anapita kutali. Ndipo anasangalala. Anamwaza ndalama zake. Anapalana ndi abwenzi. Iwo anakondwera pamodzi. Koma patapita nthawi yaing'ono ndalama zonse zinatsirizidwa. Anzake anamsiya mnyamata. Iwo sanali abwenzi abwino. Anafuna kusangalala cabe.
Mnyamatayo anaganiza, 'Tsono ndiyenera kugwira nchito. Ndifunika kukhala ndi ndalama zogula cakudya'. Anamva njala. Ndipo sanali wolimba mtima kupita kunyumba.
Iye anapeza wosungira nkhumba womwe anati, 'Mululedwa kuweta nkhumba zanga'. Nchitoyo sinali nchito yabwino. Mnyamata anali wosakondwera kwambiri. Koma kunalibe munthu wolabadira. Kunalibe womvera cisoni pa iye. Kunalibe wompatsa cakudya cabwino. O, mnyamata analakalaka kukhala kunyumba kwake ndi tate wake!
Masiku onse anaganiza za nyumba yake ndi za tate wake. Anadziwa kuti ngakhale anchito a kunyumba anali ndi cakudya cokwanira. Koma iye sanalimbe mtima kubwererako. Anaganiza kuti tate wake angakalipe kwambiri, cifukwa ca makhalidwe oipa ake.
Tsono, tsiku lina mnyamatayo anaganiza, 'Ndi cifukwa ciani ndimakhala kuno? Ndine wosakondwa kwambiri! Ndibwerere kunyumba! Ndipo ndidzauza tate wanga kuti ndinacimwa. Ndidzamuuza kuti ndikumva cisoni kwambiri. Mwina angandikhululukire ndi kundilola kukhala m'modzi wa anchito ake.'
Ndiye mnyamatayo anayambapo kupita kunyumba.
Koma mudziwa zimene zinacitika kodi?
Tate wa mnyamatayo adaganizira mwana wake wa mwamuna nthawi zonse. Adamkondabe. Masiku onse ankapita pa njira nayembekeza kuti mwana wake angabwerere kunyumba. Ndiye tate anaona mwana wake wobwerera, ngakhale iye anali kutali. Tate anathamanga kukomana ndi mwana wake wa mwamuna. Anamgwira. Anakondwera kwambiri pomuona.
Mnyamata analira, 'Atate wanga, Ndinacimwa!'
Ndipo tate anamukhululukira. Anakonda kwambiri mwana wake. Anauza anchito ake kukonzekera cakudya cabwino kuti onse akondwerere kubwereranso kwa mwana wake wa mwamuna.
Mulungu ndi monga tate uyo. Ngati tikumva cisoni pa macimo athu, atikhululukira. Akondwera pamene tibwerera kwa Iye, cifukwa atikonda.

**Kukambirana**
1. Fotokozani njira m'mene tiri monga mnyamata m'nkhani.
2. Ndi cifukwa ciani tate anakondwera kwambiri poona mwana wake?
3. Kodi tingabwerere motani kwa Mulungu Atate?
4. Kodi mumamva cisoni pa macimo anu? Mumaulula macimo anu kodi?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Ife ndife ocimwa ocoka pa maso panu. Tidziwa kuti ocimwa sangakhale ana anu. Koma tikuyamikani kuti ndinu wabwino ndi wokhululukira. Zikomo kwambiri kuti mulandira aliyense woulula macimo ake ndi wakumva cisoni pa macimo ake. M'dzina la Yesu tikuphempani izi. Amen.

## 2. Tiyenera kudziwa njira

*Yesu ananena naye, Ine ndine Njira, ndi Coonadi, ndi Moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine – Yohane 14.6*

**Kuwerenga**
Yohane 14.1-6

**Malongosoledwe**
Ngati munthu wocimwa afuna kubwerera kwa Mulungu, iye ayenera kudziwa njira.
Kumbukirani nthano ya mnyamata wosiya nyumba yake. Pamene anamva cisoni nafuna kubwerera kunyumba, iye anayenera kukhala wotsimikiza kuti ayenda pa njira yopitadi kunyumba, iai? Ifenso tiyenera kupita pa njira yoyenera tikapita kunyumba kwa Atate athu Kumwamba. Ngati tipita pa njira yosayenera, sitidzafika kunyumba. Tidzatayika.
Anthu ocimwa osabwerera kwa Mulungu m'njira yoyenera ndiwo otayika mpaka muyayaya. Ico ndi coipa coposa. Baibulo likamba kuti Yesu ndi njira yoyenera ya kwa Mulungu. Kulibe njira koma Yesu Yekha. Yesu ananena ico kwa ophunzira ake, Iye asanapite Kumwamba.
Yesu ndi ophunzira ake anakhala pa tebulo lalikulu. Anatsiriza cakudya ca madzulo. Ndipo ico cinali cakudya cotsirizira comwe anadya pamodzi pakuti Yesu adanena nao, 'Ndidzapita'.
Iwo sanafune Yesu kupita. Anamva cisoni.
Yesu ananena nao, 'Mtima wanu usabvutike. Ndidzapita kwa Atate anga. Ndipo kumeneko ndidzakukonzekerani malo. Mubwerenso kukhala ndi Ine m'nyumba ya Atate anga.
Tomasi, m'modzi wa ophunzira, anati, 'Ambuye, sitidziwa njira!'
Yesu ananena, 'Ine ndine Njira… Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine'.
Kodi Yesu anatanthauza ciani? Kodi ndi motani m'mene Iye akhala Njira yopita kwa Mulungu Atate?
Ophunzira sanamvetse. Anadziwa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Koma sanamvetsetse kuti Yesu akhala bwanji Njira yopita kwa Atate. Pambuyo pake pamene Mulungu Mzimu Woyera anawathandiza kumvetsa Mau a Mulungu, iwo anamvetsa m'mene Yesu ndi Njira.
Baibulo (ndilo Mau a Mulungu) litifotokozera m'mene Mulungu anapangitsa Yesu kukhala Njira ya cipulumutso.
Kalekale Mulungu anapanga dongosolo lodabwitsa: Iye anakonzekera kupulumutsa anthu ocimwa.
Uchimo uyenera kulangidwa. Macimo onse afunika cilango cifukwa ndiwo otsutsana ndi Mulungu. Anthu onse acimwira Mulungu wamkulu ndi woyera, ndiye anthu onse ayenera kulangidwa muyayaya. Koma Mulungu anakonza kutuma Yesu, Mwana wake, kuti Yesu alangidwe m'malo mwathu.
Ndiye Yesu ndi Njira ya cipulumutso.
M'maphunziro ena tidzaphunzira zina za Njira iyi ya cipulumutso.

**Kukambirana**
1. Kodi Baibulo litiuza za dongosolo lotani?
2. Mulungu afuna kupulumutsa anthu mwa cisomo. Kodi ici citanthauza ciani?
3. Ndi cifukwa ciani tikamba kuti Yesu ndi 'Njira ya cipulumutso'?
4. Kodi ndinu wopulumutsidwa ku macimo anu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu wacisomo, Tikuyamikani kuti m'Mau anu tiwerenga za Yesu Kristu Mpulumutsi. Tithandizeni kumvetsetsa Baibulo ndi kulisunga m'mitima yathu kuti tidziwe Njira ya cipulumutso. Tikupemphani izi zonse m'dzina la Yesu, pakuti mwa Iye tilandire cipulumutso. Amen.

# 3. Tiyenera kukhulupirira kuti Yesu ndi Mpulumutsi wathu

*Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi apabanja ako - Macitidwe a Atumwi 16.31*

**Kuwerenga**
Macitidwe a Atumwi 16.25-34

**Malongosoledwe**
Tinaphunzira kale kuti tiyenera kuulula macimo athu tisanasanduke ana a Mulungu. Tiyenera kudziwa kuti ndife ocimwa. Tiyenera kuuza Mulungu kuti tikumva cisoni pa macimo athu.
Tinaphunziranso kuti tikhoza kupita kwa Mulungu mwa Yesu yekha. Yesu anatiuza kuti Iye ndiye Njira ya kwa Atate Kumwamba.
Kodi ndi motani m'mene Yesu ndi Njira?
Iye ndiye Njira pakuti Iye yekha ndi Mpulumutsi. Tiyenera kumkhulupirira.
Kodi kukhulupirira Yesu monga Mpulumutsi wathu kutanthauza ciani?
Ico citanthauza kuti tiyenera kukhala otsimikiza munsi m'mitima yathu kuti Iye anatifera ndiponso kuti Atate anatikhululukira macimo athu onse. Ine ndiyenera kukhulupirira kuti Yesu anandifera. Inu muyenera kukhala otsimikiza kuti anakuferani.
Kukhulupirira kutanthauza kuti tiyenera kukhala otsimikiza kuti Yesu ali Kumwamba kutiyang'anira ndi kutikonda. Kutanthauzanso kuti tizimkhulupirira kuti atisamalira nthawi zonse (ngakhale nthawi ya imfa) ndiponso kuti adzatitengera Kumwamba tikamwalira.
Colinga ca Yesu pobwera pa dziko lapansi ndico kukhala Mpulumutsi wathu. Angelo Kumwamba anaimba pamene Yesu anabadwa. Anakondwera kwambiri kuti Yesu anadza kupulumutsa anthu ocimwa. Ngakhale Yesu asanabadwe, Mulungu anatuma mngelo m'modzi kuuza Mariya, mai wake wa Yesu, kuti Yesu adzakhala Mpulumutsi.
Mariya anali namwali wokhala m'mzinda wamg'ono wochedwa Nazarete. Tsiku lina mwadzidzidzi Mariya anaona mngelo wochedwa Gabrieli. Ndipo anaopa.
Mngelo ananena naye, 'Musaope. Wapeza cisomo ndi Mulungu. Mudzakhala ndi Mwana: Mwana wa mwamuna. Ndipo dzina lake ndi Yesu lotanthauza Mpulumutsi.'
Mulungu anapatsa Yesu dzina ilo, pakuti Mulungu anamtuma kukhala Mpulumutsi wathu.
Kenaka mngelo anapita kwa Yosefe. Yosefe anali mwamuna wopalana ubwenzi ndi Mariya. Mngelo anauzanso Yosefe kuti dzina la Mwana liyenera kukhala Yesu lotanthauza Mpulumutsi. Mngelo analankhula ndi Yosefe m'loto. Anati, 'Mariya adzakhala ndi Mwana ndipo muyenera kucha Mwanayo Yesu, pakuti Iye adzapulumutsa anthu ake ku macimo ao.' Kupulumutsa anthu ake ku macimo ao ndiko colinga ca kubwera kwa Yesu.
Pamene Yesu anabwerera Kumwamba, ophunzira ake anapita kulikonse kuuza za Iye. Ananena kwa anthu m'malo osiyansiyana, 'Muyenera kukhulupirira Yesu. Anabwera kucotsa macimo athu.'
Ife tiopa pamene tiganizirako kusowa kwathu, kucimwa kwathu ndi ciyero ca Mulungu. Koma ngati tikhulupirira mwa Yesu sitiyenerabe kuopa.
Iye atipulumutsa. Mulungu atikhululukira macimo athu onse cifukwa ca Yesu. Yesu ayeretsa mitima yathu kotero kuti tsiku lina sitidzacimwabe. Tidzakhala oyera ndi opanda chimo. Tidzakhala pamodzi ndi Yesu ndi Atate Kumwamba.

**Kukambirana**
1. Kodi dzina la Yesu litanthauza ciani?
2. Kodi Yesu ndi Mpulumutsi wa yani?
3. Kukhulupirira si kuganiza cabe koma kudalira pa Yesu ndi kukhala otsimikiza kuti atipulumutsa ku macimo athu. Kodi mumakhulupirira kotero?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu, Tikuyamikani kuti munatuma Yesu kukhala Mpulumutsi. Mulungu Mzimu Woyera, titsimikizeni kuti aliyense pa yekha adalire pa Yesu Mpulumutsi. Tikupemphani mwa cisomo. Amen.

# 4. Tiyenera kubadwa mwatsopano

*Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu – Yohane 3.3*

**Kuwerenga**
Yohane 3.1-5

**Malongosoledwe**
Anthu ambiri amakonda tsiku la kubadwa kwao. Tsiku limenelo ndi tsiku lokondweretsa.
Koma mudziwa kuti muyenera kubadwa mwatsopano kodi? Yesu ananena tero.
Kunali munthu wochedwa Nikodemo amene anafuna kuona Yesu usiku. Anafuna kulankhula ndi Yesu za Mulungu ndi Ufumu wa Mulungu.
Yesu anati kwa Nikodemo, 'Kulibe munthu amene angaone Ufumu wa Mulungu ngati sabadwa mwatsopano'.
Nikodemo anaganiza kuti mau awo ndi osazolowereka. Sanamvetse konse.
Nikodemo ananena, 'Ndine munthu wamkulu. Kodi ndingabadwenso bwanji? Kodi munthu wamkulu angakhalenso mwana wamng'ono?'
Yesu anati, 'Munthu wosabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa Ufumu wa Mulungu'.
Kodi Yesu anatanthauza ciani?
Tiyeni tiyese kumvetsera mau a Yesu.
Tinaphunzira kale kuti tinabadwa ndi mitima yocimwa. Tifunika mitima yatsopano. Tinaphunzira kuti tiyenera kuulula macimo athu. Tiyenera kuuza Mulungu kuti tikumva cisoni pa macimo athu. Tinaphunziranso kuti tikhoza kupita kwa Mulungu mwa Yesu, cifukwa kulibe njira ina koma Yesu yekha. Tinaphunzira kuti tiyenera kukhulupirira Yesu. Tiyenera kukhulupirira kuti anatifera pa mtanda kuti macimo athu akhululukidwe.  Koma mudziwa kodi, kuti sitikwaniritsa kucita tero? Uchimo ndi wamphamvu kwambiri m'mitima yathu kotero kuti sitikhoza kusanduka kukhala ana a Mulungu. Koma ngati Mulungu Mzimu Woyera agwira nchito m'mitima yathu, Iye atisandutsa kukhala ana a Mulungu.
Mzimu Woyera atipangitsa kukhala acisoni pa macimo athu. Mzimu Woyera atithandiza kumvetsa kuti Yesu ndi Njira yeni-yeni yobwerera kwa Mulungu Atate Kumwamba. Mzimu Woyera atipatsa cikhulupiriro m'mitima yathu kuti tikhulupirira Yesu monga Mpulumutsi wathu.
Pamene Mzimu Woyera acita nchito izo, atipatsa mitima yatsopano. Mtima watsopano ndi mtima womwe sufuna kucimwa. Ndi mtima wokonda Mulungu. Ndi mtima womwe ufuna kukondweretsa Mulungu ndi kufunsa, 'Wokondedwa Mulungu wa Kumwamba, mufuna kuti ndicita ciani?' M'njira imeneyi ife ndife obadwa mwatsopano ndiponso ana a Mulungu. Ngati Mulungu Mzimu Woyera atipatsa mtima watsopano, ife ndife tipezeka m'Ufumu wa Mulungu. Mitima yatsopano ndi mitima yosankha kucita cifuniro ca Mulungu.
Kodi mufunadi kucita cifuniro ca Mulungu?

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani tifunika mitima yatsopano?
2. Kodi tilandira bwanji mitima yatsopano?
3. Kodi tidziwa bwanji ngati tiri ndi mitima yatsopano?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Mzimu Woyera, Tipatseni mitima yatsopano kuti tikhale ana a Mulungu. Tikulemekezani kuti ndinu wamphamvu wuposa mitima yathu yocimwa. Ciyembekezo cathu ciri pa Inu, Mulungu! M'dzina la Yesu tikuphemphani izi. Amen.

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

| | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1 | 14 | 1 | 11 | 21 | 16 | 1 | 20 | 19 | 1 | 14 | 9 |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 13 | 15 | 25 | 15 |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 16 | 15 | 11 | 8 | 1 | 12 | 1 |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| 13 | 21 | 14 | 1 | 12 | 9 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| 1 | 11 | 21 | 6 | 1 |

| | | |
|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 26 | 15 | 12 | 1 | 11 | 23 | 1 |

| | | |
|---|---|---|
| 14 | 4 | 9 |

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| 26 | 15 | 3 | 9 | 13 | 23 | 1 |

| | | | |
|---|---|---|---|
| 26 | 1 | 14 | 21 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **A** 1 | **B** 2 | **C** 3 | **D** 4 | **E** 5 | **F** 6 | **G** 7 | **H** 8 | **I** 9 | **J** 10 | **K** 11 | **L** 12 | **M** 13 |
| **N** 14 | **O** 15 | **P** 16 | **Q** 17 | **R** 18 | **S** 19 | **T** 20 | **U** 21 | **V** 22 | **W** 23 | **X** 24 | **Y** 25 | **Z** 26 |

Lembani yankho la sewero:

.................................................................................................................................................

.................................................................................................................................................

Aefeso 2.1

Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace

Yohane 1.12